

Kulemba za Nsangulutso
(Creative Writing)



International
Labour
Organization

TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga**

Kulemba za Nsangulutso

Kabukuka ndi kamodzi mwa maphunziro a TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa angathe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa nkhanza kwa ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabuku kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI–Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Mchitidwe Olemba Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Office (ILO), Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4


Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:
International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Office (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kupeka ndi kulemba nkhani yosavuta. Kulembankhaniya mchitidwe olemba ntchito ana ang'ono pogwiritsa ntchito njira imeneyi.



Phindu: Kuphunzitsa luso lolemba nkhani komanso kufalitsa mauthenga. Luso limeneli limathandiza kuti ana akhale omasuka ndi kunena zomwe zili mu mtima mwawo. Phunziroli likuonjeranso pa zomwe zikuphunzitsidwa mu Phunziro la Zisudzo.



Nthawi

Maphunziro awiri azigawo ziwiri (mphindi 160)

Chilimbikitso

Ndizodabwitsa kuti masiku ano luso lolemba nkhani likuchepa ngakhale kuti dziko la pansi latukuka pa nkhani yofalitsa ndi kupezeka kwa mauthenga kapena nkhani. Masiku ano makina a kompyuta amachita zinthu zambiri zomwe kale anthu olemba amayenera kuchita okha pogwiritsa ntchito lusolawo monga kutsatira bwino malamulo a chilankhulo. Nthawi zina makinawa akumathandiza ngakhale kulemba nkhani kumene pogwiritsa ntchito njira yomutsogolera munthu pomufunsa mafunso a komwe nkhani yake ikulowera. Izipangitsa achinyamata ambiri kukhala opanda luso lopeka ndi kulemba nkhani.



Ena mwa maphunziro a TIMVERENI ndi okhudza luso la zithunzi. Kuonjezera pamenepo, achinyamata ayenera kudziwa bwino kulemba mwaluso. Achinyamata ayenera kukhala ndi luso lokwanira pa nkhaniyi kuti adzitha kupeka ndi kulemba mwaluso pogwiritsa ntchito nzeru zawo osati kukhala omangodalira zipangizo zina monga makina a kompyuta.



Achinyamata angathe kupeka ndi kulemba bwino nkhani za kuipa kwa mchitidwe olemba ana ntchito ngati apatsidwa chithandizo ndi mpata okwanira. Izi zingathandize kuti achinyamata anzawo pa dziko lonse amvetse bwino za vuto limeneli. Iwo angathe kulemba nkhani zosiyanasiyana zothandiza kupeza chithandizo komanso kulimbikitsa ena kuti atenge nawo mbali pa ntchito yolimbana ndi mchitidwe olemba ana ntchito.

Kukhala ndi luso lolemba mwaufulu zingapangitse kuti achinyamata akhale omasuka. Magawo ena andondomeko y a maphunzirowa akuphunzitsa achinyamata kulemba mwaluso masewero a zisudzo, nyimbo, makalata komanso zidziwitso zosiyanasiyana za munyuzipepala. Cholinga cha phunziro ili ndi kuzamitsa nzeru za achinyamata pa malamulo a kulemba komanso kulemba mwaluso. Tikufuna iwo adzitha kulemba maganizo awo ndi zomwe akumva pa pepala. Mu phunziroli tikulimbikitsa achinyamata kulemba ngakhale zomwe zinawachitikira mu njira yogwiritsa ntchito maina opeka a anthu ena ngati njira yofotokoza zomwe iwo akuganiza ndi kumva m'thupi mwawo.

Achinyamata ambiri sadziwa kuti ali ndi luso lolemba lo badwa nalo. Zimakhala zosangalatsa kuwaona iwo akuzindikira ndi kugwiritsa ntchito lusoli. Ngati ana akumasuka ndi kuyamba kugwiritsa ntchito luso limeli ndiye kuti ana ambiri adzakwanitsa kuchoka mu mavuto obwera chifukwa cha mchitidwe olemba ntchito ana.

Nthawi zambiri achinyamata sapatsidwa mpata otenga mbali pa zinthu zofunika. Dziko lingathe kupindula ngati achinyamata apatsidwa mpata wotenga nawo gawo pa zinthu za chitukuko. Phunziro ili likuwapatsa mwayi achinyamata kudzera mu njira ziwiri. Njira yoyamba ndi kuti afufuze mwa iwo eni luso lopeka ndi kufotokozero nkhani. Mu njira yachiwiri iwo akupatsidwa udindo wofotokoza za vuto la mchitidwe olemba ntchito ana kwa anzawo komanso onse oyimira midzi yawo kudzera mu luso lolemba.

Phunziro ili likuthandiza achinyamata kuti azamitse nzeru zawo komanso kumanga magulu awo kuti akhale ogwirizana. Kumapeto aphunziroli mudzatha kudziwa luso ndi khalidwe la achinyamata a gulu lanu. Mudzatha kuwonanso luso lawola utsogoleri, m'gwirizano wawo komanso momwe amachezera. Mudzakhalanso a chidwi kuwona momwe achinyamatawa akufotokozero malingaliro awo mu zomwe akulemba.

Kukonzekera

Pokonzekera phunziroli muyenera kuganizira ngati mudzakwanitse kuchita zonse nokha kapena mudzafuna munthu wina (odziwa bwino kulemba za nsangulutso) kuti akuthandizeni.

Ngati mwafuna kuchita zonse nokha muyenera kukonzekera mokwanira posonkhanitsa mabuku pa mutu umenewu. Mabukuwa mungathe kuwapeza mu nyumba zowerengeramo komanso sitolo za mabuku.

Mu gawo loyamba la zochita, muyenera kukhala ndi buku lofotokoza bwino za ndakatulo. Mungathe kupeza bukuli ku nyumba yowerengerako mabuku. Mukhale ndi nthawi yokwanira bwino kuti mupeze ndakatulo zolembedwa bwino.



Chidziwitso

Pozindikira kuti phunziro limeneli ndi pomwe pagona malangizo ofunika kwambiri pa zochitika zambiri za mu pulojekitiyi, yesetsani kupeza chithandizo kwa ena odziwa bwino za kulemba mwaluso kuti akutsogolereni mu phunziro limeneli. Izi zidzakuthandizani kuti musavutike ndi zochitika mu maphunziro ena a mu pulojekitiyi. Choncho gwiritsani nchito zonse zomwe zingathandize kuti muzamitse nzeru zanu



Ngati muli ndi m'nzanu amene ali odziwa bwino za kulemba mwa luso kapena aphunzitsi omwe ndi okonzeka kukutsogolerani, apempheni kuti akuthandizeni pa phunziroli. **Kupeza chithandizo**

Mungathenso kupeza chithandizo ku mabungwe ena monga bungwe la alembi. Mabungwe ngati amenewa amakhala ndi anthu ongodzipereka omwe angathandize gulu lanu pa momwe mungapititsire patsogolo luso la kupekandi kulemba nkhani.

Poganizira msinkhu wa anthu a gulu lanu, pemphani amene amalemba nkhani kapena mabuku okhudza achinyamata kuti akudzakuthandizeni. Iwo ndi amene angathe kukuthandizani mokwanira chifukwa akudziwa kale zambiri zokhudza achinyamata. Nthawi zambiri kulemba kapena kulakatula zinthu zaluso kumakhala kovuta chifukwa achinyamata ena amakhala ndi manyazi. Choncho ndi kofunika kuwalimbikitsa ndi kuwathandiza pa nthawi imene iwo akusula luso lawo lofotokoza maganizo awo polemba. Alimbikitseninsu kuti asakhale ndi manyazi kapena kuopa kuti angasekedwe pa maganizo omwe iwo angalembe.

Chifukwa cha kufunika kwa ntchitoyi, anthu ambiri ndiokonzeka kukuthandizani mwaulere. Chofunika kuchita ndi kukambirana ndi eni bungwelo kuti akuganizireni mwa padera. Ngakhale chithandizo chaulere ndi chotheke, siakatswiri onse a zolembalemba omwe angakwanitse kukuthandizani mwaulere chifukwa kapezedwe ka ndalama ndikosiyanasiyana. Choncho sibwino kuwakakamiza kuti akuthandizeni mwaulere. Mungathenso kusaka ndalama ku mabungwe kapena kwa anthu ena kuti mulipirire mlembe amene angakuthandizeni pa phunziroli. Kusaka ndalama ndi luso lofunika kwa achinyamata. Choncho konzani bwino ndondomeko ya zinthu zofunika ndi kupereka kwa anthu omwe angathandize ndi ndalama. Achinyamata ambiri amakhala ndi chidwi kuthandiza pa zinthu ngati zimenezi ndipo angakondwe kuwona ntchito zawo zitabala zipatso.

Zofunikira

- ✓ Mapepala ndi pensulo (zolemba)
- ✓ Buku la ndakatulo
- ✓ Bolodi



Kuyamba

Njira yomwe mungatsate ingathe kutsata zina mwa zinthu izi:

- Ngati mwayitana mlangizi odzakutsogolerani pa phunziroli;
- Ngati mwapeza nzanu kapena m'phunzitsi yemwe ndi odziwa bwino za kulemba yemwe wakonzeka kudzathandiza pa phunziroli;
- Ngati mwapeza mabuku okwanira pa phunziroli.



Mungathe kukwaniritsabe phunziroli ngakhale zina mwa zomwe ziri pa mwambazi zitasowa. Komabe yesetsani kukwaniritsa zina mwa zimenezi.

Cholinga chenicheni ndi chakuti achinyamata aphunzire kufalitsa uthenga mwa iwo okha osadalira gulu nthawi zonse. Komabe pachiyambi, ndi koyenera kuti achite phunziroli mu magulu a anthu awiri, atatu kapena anayi koma osapitirira pamenepo. Zochita mu phunziroli zithandiza kuti achinyamata akhale odzikhulupirira kuti angathe kuyamba kuzamitsa luso lawo lolemba nkhanu kapena nthano.

Kulongosola ntchito za gulu

Ngati achinyamatawa akonzeka kuchita zinthu payekha-payekha, onse alowe mkalasi m'mene aliyense angakhale ndi malo olembapo komanso zolemba. Yesetsani kuti aliyense akhale ndi malo ayekha kuti alembe bwino.





Chidziwitso

Njira zomwe tapereka mu phunziroli sizingafunike kwambiri ngati mwapeza munthu okuthandizani. Komabe zina mwa njirazi zingathe kugwiritsidwa ntchito. Koma ngati mukupanga zonse panokha ndipo mulibe luso lokwanira pa nkhani za kulemba, muyenera kumvetsetsa bwino zomwezalembedwa mu phunziroli.

Mungathe kusankhapo limodzi mwa maphunziro a ndakatulo “kapena „ndondomeko ya kalembedwe” kapenanso mungathe kungochita maphunziro onse motsatana.

Gawo loyamba la zochita: Kugwiritsa ntchito mawu omveka mofanana mu ndakatulo

Mphindi makumi awiri (kapena theka la nthawi ya phunziro limodzi)

Chiyambi chabwino cha phunziro la kulemba mwa luso ndi kuthetsa maganizo akuti kulemba ndi ntchito yovuta kwambiri. Achinyamata ambiri amaganiza kuti sangalembe zinthu zina koma makalata kwa anzawo kapena abale awo. Sakhulupirira kuti angathe kulemba zinthu monga ndakatulo.

Luso losavuta kuphunzira polemba ndakatulo ndi kulemba mawu omveka mofanana mu ndakatulo kapena mu nyimbo (**rhymes**). Choncho mungathe kuyamba ndikuwerenga ndakatulo zokhala ndi mawu ofanana kamvekedwe.

Chitsanzo: ndinapita ku Dowa

Kukagula ndowa

Yoyikamo mowa

Koma ndapeza bowa

Odzaza ndowa

Ndakatululo ngati zimenezi ndizosavuta kupeka ngakhalekulakatula. Mudzaona kuti achinyamata ambiri adzakhala

osangalala kutenga nawo mbali pa ndakatulozi. Choncho mkati mowerenga ndakatulozi afotokozereni kuti chilankhulo cha mu ndakatulo ngati zimenezi ndi chosavuta komanso kuti malamulo a kalembedwe amakhala ofewa kusiyana ndi zolemba zina. Pa nthawi awuzeni iwo kuti asamangike ndi malamulo a chilankhulo. Chidwi chawo chikhale pa mawu omveka mofanana. Izi zidzathandiza kuti kulemba ndakatulo kukhale kosavuta. Komabe awuzeninso kuti malamulo a chilankhulo ndi kalembedwe ndi ofunika kwambiri mu ndakatulo zozama.



Mukamaliza kufotokoza za mawu omveka mofanana mu ndakatulo komanso kuwerenga zitsanzo, awuzeni kuti tsopano muyamba kupeka mawu omveka mofana mu ndakatulo. Fotokozani kuti mawu ambiri omveka mofananawa amapezeka mu zigawo za mizere iwiri kapena inayi ya ndakatulo mu liwula kumapeto kwa mzere. Zitsanzo zina za zimenezi muzipeza mu Gawo loyamba la zowonjezera (**Annex 1**).

Mukamaliza kuchita izi ndi gulu lonse funsani achinyamatawa kuti ayesere kupeka ndakatulo zawo zokhala ndi mawu omveka mofanana. Awuzeni kuti ayambe ndi kuyesera zimezi ndi ndakatulo ya zigawo za mizere iwiri yokha. Pali njira ziwiri zimene angathe kutsata:

- Funsani gulu lililonse kuti lipereke mawu akumapeto kwa mzere kenako apange chiganizo chokhala ndi mawu amenewa kumapeto kwake.
- Gulu lonse lipereke mawu amodzi akumapeto kwa chiganizo kenako magulu onse apereke zitsanzo za ziganizo zokhala ndi mawu amenewa kumapeto kwake.

Musapereke nthawi yochuluka kwambiri kwa gulu kuti achite zimenezi. Zitsanzo zimenezi zima funika kuperekedwa mwachangu. Yenderani magulu onse ndi kuwathandiza pamene akufunika chithandizo. Mofuula, perekani malangizo komanso zitsanzo zomwe iwo angasankhepo pokonza ziganizo zawo.


Ngati nkofunika, chititsani mpikisano kuti muone amene angakwanitse kuchita bwino kuposa anzawo motere:

- Mphotho ya omaliza mwansanga kuposa anzawo.
- Mphotho kwa amene gulu lonse lavomereza kuti apeka ziganizo zoposa magulu ena.

Gawo lachiwiri la zochita: Ndondomeko ya kalembedwe ka nkhani – Kutsata zigawo zinayi za nkhani

Nthawi: Mphindi makumi asanu ndi limodzi

Monga mwaona kale, pali njira zambiri zomwe mungagwiritse ntchito pofuna kuyamba kuphunzitsa za kalembedwe ka nkhani. Imodzi mwa njirazi ndiyotsata zigawo zinayi za nkhani. Njirayi ndi yosavuta ndipo ndi yodalirika kwa amene akufuna kuzamitsa luso lawo lolemba nkhani. Chithunzi chili pansipa chikuyimirira zigawo zinayi zimenezi:



Gawo lililonse likuyimira chigawo cha nkhani. Gawo 1 ndi chiyambi cha nkhani. Gawo 2 ndi 3 ndiye tsinde la nkhani (kapena pachimake pa nkhani), ndipo Gawo 4 ndi kumapetokwa nkhani. Choncho nkhani ikuyambira mu Gawo 1 kuthera mu Gawo 4. Kumbukirani kuti ndikofunika kuti ophunzira aliyense akhale omasuka pa nthawi ya phunziroli. Musanawapatse mpata wolembe nkhani pawokha, athandizeni ophunzira kulemba nkhani yachitsanzo pa bolodi potsata ndondomeko ya zigawo yomwe yaperekedwayi.

Mungathe kupereka chitsanzo chosavuta motere: mu Gawo 1 perekani dzina “kapena mwini nkhani”, fotokozani za khalidwe ndi maonekedwe ake. Ngati ndi kotheka fotokozerani zimenezi mu liwu limodzi monga okhumudwa makamaka poganizira cholinga cha pulojekitiyi. Choncho lembani mu bokosi limodzi (Gawo 1) pabolodi chitsanzo ngati “Dalitso” (dzina kapena mwini nkhani). Iye ndi “m’nyamata” (kufotokoza za mwini nkhani). Iye ndi “wokhumudwa”. Mukatero ndiye kuti mwayamba kukamba nkhani.

Popitiriza, lembani mathero a nkhani mu bokosi la Gawo 4. Mu chitsanzochi, mwini nkhani mu Gawo 4 ndi yemweyo wa mu Gawo 1 koma wosiyana m’maonekedwe chifukwa cha kusintha kwa zinthu mu moyo wake. Perekani chitsanzo china chosavuta mu Gawo 4 monga: Nkhaniyi ndi ya Dalitso. Iye adakali m’nyamatabe. Koma tsopano ndi m’nyamata “wokondwa” (maonekedwe osiyana ndi poyamba pa nkhani). Choncho nkhani ingathe kumalizidwa motero.

Mu tsinde la nkhani (Gawo 2 ndi) ndiye mwagona zonse zomwe zinamuchitikira Dalitso. Choncho lumikizani nkhani yonse mwatsatanetsatane kuchokera mu Gawo 1 mpaka Gawo 4.

Bokosi lachiwiri likupereka zinthu zomwe zapangitsa kuti “Dalitso” akhale “wokhumudwa”. Funsani gulu lanu kuti lipereke zitsanzo za zomwe zingapangitse kuti Dalitso akhale wokhumudwa, lembani zifukwa zitatu. Mwa chitsanzo gulu lingathe kupereka zifukwa monga: Alibe anzake. Ali ndi njala. Walakwa mayeso.

Potsatira ndondomeko yomweyi pitirizani nkhaniiyi poganizira zomwe zinachitika kwa “Dalitso” kuti akhale “wokondwa”. Choncho mu gawo 3 ndi momwe mungafotokoze zifukwa zomwe zapangitsa kuti Dalitso akhale “wokondwa”. Funsani gulu kuti liperekenso zifukwa ndipo lembani mu bokosi lachitatu zifukwa zitatu za chitsanzo monga: Wapeza anzake. Wapeza chakudya. Wakhoza mayeso. Izi zikusonyeza kusiyana ndi zomwe zinalembedwa mu bokosi lachiwiri.

Mukafika pamenepa ndiye kuti mwamanga makwelero a nkhani yanu. Mungathe kuwonjezerapo zinthu zina zopangitsa kuti nkhani yanu ikome.

Kuwonjerapo ziganizo zina mu mabokosiwa kudzathandiza kuti nkhaniiimveke bwino. Mungathe kuwonjezera ziganizo mu nkhani poyankha mafunso awa mu mabokosi onse: Ndani? Chiyani? Zinachitika liti? Kuti? Chifukwa chiyani? komanso Bwanji? Mukatero lumikizani ziganizo zonse momveka bwino. Potsatira chitsanzo chaperekedwa chija, mungathe kufunsa mafunso monga: Kodi Dalitso amakhala kuti? Chifukwa chiyani Dalitso analakwa mayeso? Ndani anamuthandiza Dalitso? Anamuthandiza bwanji? Anzake a Dalitso anachita chiyani atamva izi? Kodi zimenezi zinachitika liti/nthawi yanji? Pitirizani kufunsa mafunso ngati amenewa ngati mukufunabe kuwonjezera ziganizo mu nkhani. Koma pa nthawi ya maphunzirowa sikofunika kusalikitsa nkhani kwambiri.



Mukamaliza chitsanzo chilli pamwambachi gawani magulu angapo ndikuwapatsa mutu wa nkhani kuti awukulitse potsatira ndondomeko ya mabokosi anayi aja. Mupereke nthawi yongokwanira kuchita izi. Mungathe kusankhana kuwapatsa mutu wa nkhani komanso maguluwa angathe kukambirana okha ndi kupeza mutu wao wankhani. Bokosi loyamba mungathe kukhala "Chimwemwe ndi mtsikana wasangalala". Bokosi lachinayi mukhale "Chimwemwe ndi mtsikana wasangalala". Awuzeni am'magulu kuti amalizitse nkhanayi polemba ziganizo mu bokosi lachiwiri ndi lachitatu. Awuzeninso kuti angathe kusalikitsa nkhani yawo poyankha mafunso ngati aperekedwa pamwambawa.

Mphindi zisanu kapena khumi ndi zokwanira koma osapitirira pamenepo. Alimbikitseni achinyamatawa kugwiritsa ntchito nthawi yochepa komanso kuti akhale omasuka. Nthawi yoperekedwa ikatha, awuzeni kuti awerenge nkhani zomwe alemba.

Ntchitoyi ingagwiridwe mwachangu komanso mwansangala ngati mutachititsa mpikisano wofuna kupeza:

- Nkhani yoseketsa kwambiri yomwe yalembedwa munthawi yololedwa.
- Nkhani yabwino kwambiri yomwe yalembedwa munthawi yololedwa.

Gawo lachitatu la zochita: Nkhani ya mwana wa pantchito

Phunziro limodzi

Kumapeto a gawo la chiwiri la zochita, achinyamata ayenera kukhala ndi chidwi cholembe nkhani pozindikira kuti kulemba nkhani mwaluso ndi ntchito yovuta kwambiri. Tsopanondinthatiwolembe nkhanipankhani za ana ogwira antchito (child labourers). Mu gawo ili aliyense akhale ngati momwe amakhala mkalasi ndipo aliyense akhale pomasuka kuti alembe bwino. Ndi bwino kuchita zochitika za mu gawo ili aliyense payekha koma ngati ndi kofunika magulu ang'onoang'ono ndi oloedwa. Mwa chitsanzo, amene ali ndi mavuto monga ophunzira mochedwa (pang'ono-pang'ono) ngakhale osadziwa kulemba ndi kuwerenga angathe kuyikidwa mu magulu kuti atenge nawo mbali mu zochitikazi. Nthawi zonse khalani atcheru ndi kuwaganizira anthu ngati amenewa.

Funsani aliyense kuti alembe nkhani ya ana apatchito. Mungathe kuchita izi potsatira imodzi mwa njira izi:

- Aliyense asankhe dzina, zaka komanso maganizo a mwana wapantchito mu bokosi loyamba ndi kuperekanso maganizo a momwe mwanayu akuwonekera mu bokosi lachinayi.
- Ndi gulu lonse, lembani ziganizo za mu bokosi loyamba komanso lachinayi ndi cholinga chakuti aliyense alembe nkhani ya mwana yemwe aliyense wamulemba mu nkhani.
- Kulola kuti onse a mu gulu asankhe kutsata njira yawo kapena kutsata njira yomwe mwawapatsa mosasiyana ndi ena.



Fotokozani kwa gulu kuti nthawi zina kawonekedwe ka munthu mu bokosi loyamba kangathe kukhala kofanana ndi momwe akuwonekera mu bokosi lachinayi chifukwa ndi zotheka munthu kukhala okhumudwa pa chiyambi komanso kumathero a nkhani. Komabe, cholinga maphunzirowa ndi chakuti ana apatchito akhale ndi chiyembekezo. Choncho ngati mwana wa patchito ndi wokhumudwapa chiyambi cha nkhani, zikhathe kukhala zosangalatsa kumuona akusangalalako pa mathero a nkhani.

Mu gawo lachiwiri la zowonjezera (Annex 2) mwaperekedwa chitsanzo cha nkhani yothera ndi chisangalalo. Samalani pogwiritsa ntchito zitsanzo ngati zimenezi. Chofunika kwambiri ndi kuwasiya achinyamata kuti alembe ndi kufotokoza okha za m'maganizo awo. Athandizeni ndi kuwakumbutsa za mafunso othandiza kukulitsa nkhani aja. Akalimbikitsidwa kutsata njira imeneyi adzatha kulemba zinthu zambiri mu nkhani yawo ndipo akazolowera zimenezi mfundo zambiri zidzayamba kutuluka m'maganizo awo mosavuta. Kufikira pamenepa ndiye kuti munthu wazama pa ukatswiri olemba nkhani mwaluso.

Panthawi yomwe mukuwathandiza pa ntchito yawo mudzatha kuwona omwe akukwaniritsa kutulutsa mfundo mosavuta komanso omwe sakumasuka chifukwa cha mavuto osiyanasiyana a m'maganizo. Athandizeni mwapadera omwe akukanika kumasuka ndi kutulutsa mfundo za m'maganizo awo. Funsani mafunso othandiza kuti iwo amasuke. Athandizeni kuti afotokoze bwino za nkhani yawo, momwe mwini nkhani akuganizira komanso zomwe wakumana nazo. Kodi ndi m'tsikana kapena 'nyamata? Kodi iye anapezeka bwanji pamenepo/kumeneko? Kodi ali kuti? Ndi ntchito yanji yomwe akugwira? Mantha kapena manyazi amachoka ngati mafunso ngati amenewa afunsidwa, ndipo pawokha adzatha kupitiriza ndi mafunso ngati omwewa mpaka kukwaniritsa kulemba nkhani yonse bwino lomwe.

Ena amanena kuti ndi chapafupi kulemba nkhani ngati olemba "atasandulika" ngati iye ndi amene ali mu nkhaniyi. Choncho iye amakhala ngati chojambulira kanema. Ganizirani kanema ikuyamba. Inuyo mukhale ngati chojambulira zithunzi za kanema ndipo muzinena zomwe zikuchitika. Kodi mwini nkhani wayima pati? Nanga wayima motani? Ngati kuli mdima, ndichifukwa chiyani? Kodi ndi masana kapena usiku ndipo ndi nthawi yanji? Kodi mwini nkhani ndi okhumudwa? Kodi akulira? Kodi akulira chamumtima? Kodi wavulala?

Tsopano mungathe kudziwa kuti achinyamatawa atengeka ndipo maganizo awo onse akodwa mu kulemba. Mungazindikire izi powona momwe iwo akugwirira ntchito yomwe mwawapatsa, kuwala kwa maso awo polingalira zomwe akuwona m'maganizo awo pa nkhani yofanizirayi. Mudzakhala odabwa kuwona momwe achinyamatawa angasinthikire. Mwina iwo pawokha sangazindikire kuti akusintho, koma inu mungathe kuwona za kusinthaku. Mudzakhala okondwa pozindikira kuti mwathandiza kuti izi zichitike.

Mungathe kuwonjezera nthawi kuti anthu amalize nkhani zawo, koma sikofunika kuti zochitikazi zitenge nthawi yayitali kwambiri. Nkhanizi zingakhale ndi "tanthauzo" ngati zimalizidwa mu nthawi yochepa powopetsa kuchulutsa zonena.

Zoyenera kuchita ndi zoyenera kupewa

Onetsetsani kuti aliyense akutenga nawo mbali. Achinyamata ena ndi amanyazi komanso mantha choncho gwiritsani ntchito zochitika mu phunziroli kuti aliyense akhale omasuka ndi kutenga nawo mbali. Onetsetsani kuti aliyense walembako kanthu, kangachepe.



Gwiritsani ntchito nthabwala komanso zoselewulana kuti gulu limasukirane. Phunziroli ndilotheandiza achinyamata kukhala odzidalira, komanso ndi losangalatsa. Ambiri sangadziwe kuti aphunzira zinthu zambiri mpaka nthawi yomwe adzayambe kugwiritsa ntchito zomwe aphunzira pano ku zochitika za m'maphunziro ena komanso mu moyo wawo m'tsogolo.

Onetsetsani kuti aliyense akulemekeza maganizo a anzawo. Kunyozana kapena kugwiritsa ntchito mawu olawula sizololedwa.

Alimbikitseni achinyamatawa kuwerenga nkhani zawo ku gulu lonse. Ngati ena sakufuna kuwerenga nkhanizi kwa anzawo, musawakakamize. Ngati akufuna kuti nkhanizi zawo zikhale za chinsisi, aloleni kutero.



Sungani nkhanizi zonse zomwe gulu lalemba.

Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi

Pamene achinyamata ayamba kulemba nkhani zokhudza ana apantchito kumathero a phunziro la kulemba mwaluso ndi kofunika kuwayang'anira bwino komanso kuwathandiza mosamala. Imeneyi ndi nthawi ntchito yofunika kulimba m'maganizo chifukwa ndi ntchito yomwe ikukhudza mavuto omwe ana amakumana nawo choncho zinthu zina zingakhale zomvetisa chisoni. Mwina ena mu gulu lanu anakumanako ndi zovuta zomwe ana apantchito amakumana nazo pamene ena sanazioneko. Athandizeni onse ndi kuwalimbitsa mtima pamene akulemba za kukhosi kwawo.



Malizani zokambirana zanu pa malo a bwino opanda phokoso. Gulu likhale lomasuka kunena zomwe akumana nazo komanso zomwe akuganiza. Aloleni ena omwe angafune kuwerengankhanizawo ku gulu lonse. Aloleni kuti awerenge nkhani yawo atakhala pa malo awo kuti asamangike. Kambiranani nkhani yomwe yawerengedwa. Gulu lonse likhale ndi ufulu ofunsa mafunso pa nkhani yomwe yawerengedwa. Ndi zochititsa chidwi kudziwa zomwe zimapangitsa anthu kuti alembe za anthu omwe amapezeka mu nkhani ndiponso zomwe anthuwo amapanga. Zimenezi zimaonetsa chikhalidwe cha olemba nkhani komanso zomwe iye amaganiza. Choncho kambiranani nkhani zonse mokwanira.

Nkhani zina zingathe kukhala zolembedwa bwino komanso zochititsa chidwi kuposa zina. Onetsetsani kuti mwakambirana nkhani zonse moyenerera komanso mosakondera. Nkhani iliyonse ndiyothandiza kuti mudziwe zomwe ana akuganiza pa nkhani ya ana ogwiritsidwa ntchito.

Kambiranani ndi gulu maganizo osindikiza nkhani zomwe zalembedwa mu njira zosiyanasiiyana (onani "Kuunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo"). Mvetserani ndi kulemekeza maganizo a gulu pankhaniyi. Ngati asankha kuti mungowasungira nkhanizi, lemekezani zofuna zawo ndipo musasindikize nkhanizi. Ndikofunika kuti gulu likhale ndi chikhulupiriro ndi inu kuti akudalireni.

Ngati mwaona kutiana ena ali ndi luso lapadera polemba nkhani, apempheni kuti apitirize kulemba nkhani yawo ndi kuyimaliza mwa dongosolo. Iyi mungathe kuyitenga nkhani yachitsanzo yomwe mungayigwiritse ntchito pofalitsa mauthenga a mchitidwe olemba ntchito ana kwa anthu ambiri ndi kupititsa patsogolo pulojekiti imeneyi.

Chidziwitso

Zindikirani kuti zaluso monga nkhani zomwe zalembedwazi zingathe kugwiritsidwanso ntchito mu zochitika zina mu ndondomeko ya maphunzirowa monga Phunziro la zisudzo. Mungathe kugwiritsa ntchito zina mwa nkhani zomwe zalembedwazi popanga masewero a zisudzo. Zimenezi zidzathandiza kuti anthu amvetsetse za nkhanizi komanso kuti azindikire zomwe achinyamata angathe kuti kukwaniritse ngati apatsidwa mpata komanso kuthandizidwa mokwanira. Nkhani zimenezi ndizothandiza kuti mukwaniritse zochitika mu phunziro la zisudzo.

Choncho, sungani nkhanizi mosamala ndikuzigwiritsa ntchito mu njira zina zomwemungafune.



Kalondolondo wa zochitika



Pali zizindikiro zingapo zothandiza kudziwa ngati ntchito yayenda bwino. kumapeto a phunziroli, mwana aliyense walembe nkhanzi yake. Kupambana kwa kalembedwe ka nkhanizi kukudalira momwe anawa aphunzitsidwira, momwe inu kapena anthu ena owathandizira anawa, komanso nzeru za mwana aliyense.

Mungathe kupititsa patsogolo zomwe mwapanga pogwiritsa ntchito maganizo monga osindikiza nkhanzi zomwe zalembedwa. Nkhanizi mungaziyike mu nyuzipepala ya pa sukulu yanu, kapenanso kuzikhoma ku malo komwe kumafika anthu ambiri kuti anthu ambiri awerenge nkhanizi. Mungathenso kupeza atolankhani a m'dera lanu omwe angasindikize nkhanizi. Afunseni a ku nyuzipepala kuti mudziwe njira zomwe mungatsate. Atsimikizireni ana omwe alembe nkhanzi kuti asakhale ndi nkhanza kuti maina awo sangawululidwe ngati iwo sakufuna. Nkhanizi zingakhale zosangalatsa kwa anzawo a anawa. Makolonso angakhale ndi chidwi ndi momwe ana alembera nkhanizi, choncho ndi kofunika kuzifalitsa kwa anthu ambiri. Imeneyi ndi njira imodzi yothandiza kuti anthu ambiri azindikire komanso atenge mbali pa zochitika zokhudza ana ogwira ntchito.

Ngati njira yowaphunzitsa achinyamatawa, apatseni udindo opeza okha njira zosindikizira nkhanzi zawo. Chisankho cha komwe nkhanizi zikasindikizidwe chidzatsata momwe zinthu ziliri mu dera lanu. Ngati kusindikiza nkhanizi kungatheke, ndiye kuti ntchito yanu yayenda bwino komanso mungathe kukhala ndi chikhulupiriro kuti mauthenga anu agwira ntchito nthawi yayitali ndi kufika kwa anthu ambiri.

Pamene mwamaliza maphunziro a mu gawo limeneli, muyambe phunziro lina. Ndi bwino kupitiriza phunziro limeneli poyamba phunziro lozimitsa luso la kalembedwe monga la utolankhani (Kufalitsa Nkhanzi: Mu nyuzipepa).

Zowonjezera zoyamba (Annex 1)

Ndakatulo za nsangulutso

Njira imodzi yolembera ndakatulo za nsangulutso ndi kulemba mawu omveka mofanana kumapeto a mizere iwiri kenako ndi kumalizitsa chiganizo chonse poyambira kumapeto kupita koyambira chiganizocho.

Chitsanzo

1. bowa
2. mowa
- 1.Kodi munalawako bowa?
- 2.Owawa kuposa mowa?

Muchitsanzochi, mzere oyamba uli ndi mawu akuti “bowa” ndipo mzere wachiwiriuli ndi mawu akuti “mowa”. Mawu amenewa ndi omveka mofanana ndiponso akupezeka kumapeto achiganizo. Mwaonanso mu chitsanzo chomwechi kuti mungathe kuyamba ndakatulo yanu ya nsangulutso popanga ziganizo zothera ndi mawu amenewa koma zomveka bwino.

Inunso yesani kupeza mawu awiri omveka mofanana ndi kuwalembe pa bolodi monga mu chitsanzo chilli pamwambachi. Funsani a gulu lanu kuti apereke zitsanzo ndipo kenako mulembe ziganizo zogwirizana koma zothera ndi mawu amene mwalembe kumapeto aziganizo zanu. Awuzeni a mu gulu lanu kuti atchule zitsanzo za mawu ofanana mokweza ndipo lembani mawu amenewa pa bolodi. Chitani zimenezi momasuka komanso ndi nsangala.

Chinsinsi cha ndakatulo za nsangulutso ndi kukhala ndi mawu awiri omveka mofanana kumathero a ziganizo ziwiri. Choncho gulu lipitirize ndakatulozi ndi mawu omveka mofanana ndikuwayika ku mapeto a ziganizo. Ntchito yanungati mlangizi ndikuwathandiza anawa kuti asasokonezeke komanso kuti ziganizo zomwe zikupangidwa zikhale ndi tanthauzo. Cholinga cha ndakatulozi ndi kupanga nkhani mu ndakatulo yokhala ndi mawu omveka mofanana kumathero achiganizo.

Onaninso chitsanzo chilli m'musimu:

Tsiku lina mwana wa a Zulu

Ananyamuka kupita kusukulu

Kumeneko anakumana ndi anzake

Omwe anamulanda zinthu zake

Iye analimbana nawo

Mpaka anakafika kwawo

Ndakatuloyi ndi ya nsangulutso chabe chifukwa ilibe tanthauzo lenileni koma zomwe zikunenedwa ndizomveka. Kalembedwe ka ndakatulo zimenezi ndi kothandiza achinyamata kuganiza mozama mbali ina akuseketsana. Ndakatulo zimenezi zingagwiritsidwenso ntchito pofalitsa mauthenga ena ofunika okhudza ana monga kuponderezedwa kwa ufulu wao.

Zowonjezera zachiwiri (Annex 2)

Nkhani ya Yamikani

Nkhani ili pansiyi yalembedwa motsata ndondomeko ya mabokosi anayi yomwe ikupezeka mu Gawo lachiwiri la zochita.

Bokosi loyamba: Yamikani ali ndi zaka zisanu ndi zitatu. Bokosi lachiwiri: Iye ndiosangalala chifukwa anasiyana ndi makolo ndi abale ake. Tsopano akudwala ndiponso ndi wachisoni. Bokosi lachitatu: Anthu ena amutenga ndi kumusamalira Yamikani. Bokosi lachinayi: Yamikani akukhala kwao ndi abale ake. Tsopano iye ndiwosangalala.

Nkhaniyi tingathe kuyipitiriza powonjezera zomwe zinamuchitikira Yamikani kuchokera nthawi yomwe anasiyana ndi makolo ake ndikukalembedwa ntchito mokakamizidwa mpaka pomwe anatengedwa ndi kukumananso ndi makolo ake. Pogwiritsa ntchito njira yofunsa mafunsoi ja , tingathe kulemba nkhanu ya umphawi wa dziko lomwe Yamikani anagwirako ntchito kutali ndi abale ndi makolo ake. Patapita nthawi pang'ono Yamikani anadwala ndi kukomoka akugwira ntchito chifukwa chozunzidwa ndi abwana ake komanso banja lawo. Yamikani amayeserako kuthawa koma amalephera koma tsiku lina anathawa mpaka kufika kwawo. Mwatsoka bwana wake anazindikira za kuthawa kwake ndipo anatuma zimbalangondo kukamusaka. Anthu amenewa anamenya makolo ake ndikumutenga kukamubwezeranso ku malo antchito. Anamenyedwa kwambiri ndipo anadwala pafupifupi kufa.

Panapita nthawi akuzuzidwabe. Mwamwayi kunabwera bungwe la ufulu wa anthu lomwe linamva za kampani imeneyi yomwe imagwiritsa ntchito ana ang'ono. Bungweli limapita ku malo ngati amenewa kumakatengako ana ang'ono komanso kuonetsetsa kuti chilungamo chachitika. Anabwera usiku wa tsiku lina ndipo anatengako Yamikani ndi ana ena okwana khumi ndi asanu. Anamutengera ku chipatala ndipo atachira anapita naye kwawo.

Mwini wa kampani uja anakawonekera ku bwalo la milandu ndipo anamangidwa. Bungwe la ufulu wa anthu lija linathandiza bambo ake a Yamikani kuti ayambe bizinezi yogulitsa zipatso ndipo anayamba kuthandiza banja lawo mosavuta.

Yamikani anachira. Tsopano Yamikani ndi m'tsikana wosangalala

Zolembe zina

[illegible]

Zolembe zina

[illegible]



Lekani Kugwiritisa Ntchito Ana

ILO
International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0-1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipecc

ISBN 92-2-113240-4

